PHUNZIRO LA 18

1. Mulungu anamuwuza Nowa kuti adzatumiza chigumula cha madzi kudzaŵawononga anthu onse amene sakukhulupilira mwa Mulungu. Kodi Mulungu amayiwala zimene walankhula kuti azichita?
-Iyayi.

2. Kodi Mulungu amazichita zinthu zimene walankhula kuti azichita?
-Inde. Mthaŵi zonse Mulungu amachita zinthu zimene walankhula kuti adzazichita.

3. Kodi Mulungu anaŵadikilira anthu nthaŵi yayitali bwanji kuti iwowo akhulupilire mwa Iye?
-Zaka 120.

4. Kodi pamene Mulungu amkawadikilira anthu kuti akhulupilire mwa Iye, ukali Wake chifukwa cha machimo awo unachepa?
-Iyayi. Ukali wa Mulungu pa tchimo umangopitabe mtsogolo mpaka pa nthaŵi imene imafika kuti Iye apereke chilango pa tchimolo.

5. Kodi amene anamuwuza Nowa ndi banja lake kuti alowe m'chombo anali ndani?
Mulungu anamuwuza Nowa ndi banja lake kuti alowe mchombo

6. Kodi Nowa ndi banja lake analowa bwanji m'chombo?
-Analowa  kupitira pa khomo limodzi lokha.

7. Kodi anatseka khomo la chombo anali ndani?
-Mulungu.

8. Kodi chifukwa chiyani Mulungu anatseka chitseko?
-Kuti anthu amene anali mkati atetezedwe.
-Kuti anthu amene anali kunja kwa chombocho asathe kulowa, koma afe.

9. Kodi pali amene angathe kuthaϖa ku chilango cha Mulungu?
-Palibe.

10. Kodi Mulungu anachipangitsa bwanji kuti chigumula cha madzi chikhale pa dziko lonse la pansi?
-Mulungu anaŵapangitsa madzi onse amene anaŵayika kumwamba kuti agwe ngati mvura.

11. Kodi anthu anali atayiwonako mvura chiyambireni?
-Iyayi.

12. Kodi chinachitika ndi chiyani kwa anthu amene anali kunja kwa chombo?
-Anthu onse amene anali kunja kwa chombo anafa.

13. Kodi pali amene anafa mchombo muja?
-Iyayi.

14. Kodi chifukwa chiyani Mulungu analandira msembe ya Nowa chigumula chija chitatha?
-Chifukwa chakuti Nowa amakhulupilira mwa Mulungu.
-Chifukwa chakuti Nowa anasiya kutsatira njira yake ndikuyamba kutsatira njira ya Mulungu.

15. Kodi magazi a nyama analipira machimo a Nowa?
-Iyayi.
-Magazi a nyama amamuphunzitsa Nowa kuti chilango cha tchimo ndi imfa yosatha.



-Mulungu amkafuna kuti anthu adzadze pa dziko la pansi koma anthuwo amkafuna kuti adzikhala pa malo amodzi.

-Kodi anapambana ndi ndani pakati pa Mulungu ndi anthu?
-Mulungu.

-Kodi pali munthu amene angalimbane ndi Mulungu ndikupambana?
-Palibe.

-Kodi Mulungu adzachita chiyani kwa anthu amene akulimbana Naye?
-Mulungu adzaŵapatsa chilango.

-Mulungu anaŵabalalitsira anthu ku malo osiyanasiyana pa dziko la pansi.

-Anthu ena anapita pafupi.
-Anthu ena anapita kutali kwambiri.

-Mu zaka zambiri zapitazo, anthu akhala akupita ku malo osiyanasiyana poyenda ndi miyendo ndiponso zombo.

-Umu ndi m’mene mitundu yosiyanasiyana yinayambira.
-Umu ndi m’mene mtundu wa Chichewa unayambira.

-Makolo a Ayawo anayambira ku Babulo.

kwa anthu, kodi anthuwo bwenzi akukhala pa malo amodzi?
-Iyayi.

-Kalekale, makolo athu amkalankhula chilankhulo chimodzi.

-Koma chifukwa chakuti makolo athu sanamumvere Mulungu ndipo anakana kudzadza pa dziko lapansi, Mulungu anawapatsa zilankhulo zosiyanasiyana.

-Mulungu anawapatsa anthu zilankhulo zosiyanasiyana ku Babulo.

-Chilankhulo cha Chiyawo chinayambira ku Babulo.
-Chilankhulo cha Chichewa chinayambira ku Babulo.
-Chiyankhulo cha Chizungu chinayambira ku Babulo.

-Zilankhulo zonse zinayambira ku Babulo.

-Kodi Mulungu anachitanso chiyani atatha kuŵapatsa anthu zilankhulo zosiyanasiyana?

Tiyeni tiŵerenge Genesesi 11:8-9

8-Chomcho Mulungu anaŵabalaritsa anthu pa dziko lonse la pansi, ndipo iwowo anasiya kumanga mzinda uja.
9-Chomcho mzindawo anawupatsa dzina lakuti Babuloni, chifukwa chakuti kumeneko ndi kumene Mulungu anaŵabalaritsa anthu pa dziko lonse la pansi.

-Mulungu atatha kuŵapatsa anthu zilankhulo zosiyanasiyana, Iye anaŵabalalitsira anthu ku malo osiyanasiyana pa dziko lonse la pansi.



16. Kodi Mulungu anamupatsa Nowa pamodzi ndi anthu onse chizindikiro chotani?
-Chizindikiro cha utawaleza.

17. Kodi chizindikiro cha utawaleza chikutanthawuza chiyani?
-Chizindikiro cha utawaleza chimatanthawuza kuti Mulungu sadzawononganso dziko la pansi ndi chigumula cha madzi.

18. Kodi Mulungu anasunga chipangano Chake?
-Inde.
-Mulungu sanama.

19. Kodi ana amuna a Nowa amene ali makolo a anthu onse a padziko la pansi ndi ndani?
-Ana amuna a Nowa amene anali makolo a anthu onse pa dziko la pansi anali Semu, Hamu ndi Yafeti.

-Panapita zaka zambiri, Mulungu atatha kumupulumutsa Nowa ndi mkazi wake.
-Panapita zaka zambiri, ndipo ana ambiri anabadwa mpaka padziko la pansi panalinso anthu ambiri.

-Anthu amene anabadwa pambuyo pa Nowa ndi amene anali makolo anga ndiponso anu.

-Ngakhale kuti makolo athu amkadziwa za Mulungu, iwo ankakana kukhulupilira mwa Mulungu.

-Kodi makolo athu amkadziwa bwanji za Mulungu?
-Makolo athu amkadziwa za Mulungu chifukwa chakuti anthu akuluakulu amkawawuza anthu ang’onoang’ono za Mulungu ndi chigumula.

-Kodi anthu akuluakuluwo amkawawuza chiyani za Mulungu ndi chigumula anthu ang'onoang'ono?

-Anthu akuluakuluwo amkawawuza anthu ang'onoang'ono kuti Mulungu amadana ndi tchimo, chomcho Iye anawawononga anthu onse kupatula Nowa ndi banja lake.

-Kodi makolo athu amkadziwanso bwanji za Mulungu?

-Kachiŵiri, Makolo athu amkadziwa za Mulungu chifukwa chakuti utawaleza umkawawuza za Mulungu.

-Kodi utawaleza umkawawuza chiyani makolo athu za Mulungu?
-Utawaleza umkawawuza makolo athu kuti Mulungu amaŵakonda anthu onse ndipo sadzaliwononganso dziko la pasi ndi chigumula cha madzi.

-Kodi makolo athu amkadziwanso bwanji za Mulungu?

-Kachitatu, makolo athu amkadziwa za Mulungu chifukwa chakuti, mlengalenga, mapiri, ndi mitengo, zimkawawuza iwowo za Mulungu.

-Kodi mlengalenga, mapiri, nyanja ndi mitengo imkawawuza chiyani makoloa athu za Mulungu?

-Zimkawawuza kuti Mulungu yekha ndi Mulungu, ndipo anthu ayenera kumamutsatira Mulungu yekha.

-Kodi utawaleza amatiwuzabe za Mulungu masiku ano?
-Inde.
-Kodi mlengalenga , mapiri, nyanja ndi mitengo, zimatiwuzabe za Mulungu masiku ano?
-Inde.



-Mulungu sayiwala zimene anthu amachita.

-Kodi Mulungu anati chiyani atawona kuti anthu samkamumvera Iye?

Tiyeni tiŵerenge Genesesi 11:6-7

6-Ndipo AMBUYE anati, "Tsopano anthu onsewa ndi amodzi, ndipo akulankhula chilankhulo chimodzi. Zinthu akuchitazi ndi chiyambi chabe cha zinthu zimene adzazichite. Kenako iwowa adzachita china chilichonse chimene adzachifune.
7-Tiyeni titsikire komweko, tikasokoneze chilankhulo chawo kuti asamvane."

-Chifukwa chakuti makolo athu sanamumvere Mulungu, Mulungu anaganiza zopereka chilango kwa iwowo.

-Kodi chilango chimene Mulungu anachiganizira chinali chotani?

-Mulungu anaganiza zopereka zilankhulo zosiyanasiyana kwa anthu.

-Kodi Mulungu anakapereka zilankhulo zosiyanasiyana kwa anthu, kodi anthuwo bwenzi akumvana?
-Iyayi.

-Kodi Mulungu  anakapereka zilankhulo zosiyanasiyana kwa anthu, kodi anthuwo bwenzi atamaliza kumanga msanjayo?
-Iyayi.

-Kodi Mulungu anakapereka zilankhulo zosiyanasiyana

Tiyeni tiŵerenge Genesesi 11:5

5-Koma Ambuye anatsika kudzawona mzindawo, pamodzi ndi msanja imene amkamanga anthu ija.

-Mulungu anawona kuti anthu onse akumanga msanja yayitali.
-Mulungu amawona china chilichonse.

-Mulungu amaŵawona anthu onse kwina kulikonse.
-Mulungu amamuwona wina aliyense nthaŵi zonse.

-Mulungu amaŵadziwa maganizo a anthu onse.

-Munthu asanayambe kuganiza maganizo, Mulungu amakhala ataŵadziŵa kale maganizowo.

-Mulungu amaŵadziwa mawu a anthu onse.

-Munthu asanayambe kulankhula mawu, Mulungu amakhala ataŵadziwa kale mawuwo.

-Mulungu amazidziwa zochita za anthu onse.

-Munthu asanayambe kuchita chinthu china chilichonse, Mulungu amakhala atachidziwa kale chinthu chimene akufuna kuchichitacho.

-Anthu amkaganiza kuti Mulungu wayiwala za iwowo.
-Kodi Mulungu anayiwala za iwowo?
-Iyayi.

-Mulungu sayiwala zimene anthu akuganiza.
-Mulungu sayiwala zimene anthu amanena.



-Ngakhale kuti makolo athu amkadziwa za Mulungu, iwo amkakanabe kukhulupilira mwa Mulungu.

-Anthu ochepa okha ndi amene amkakhulupilira mwa Mulungu.

-Ambiri mwa makolo athu amkalamuliridwa ndi Satana.

-M'malo momutsatira Mulungu, ambiri mwa makolo athu amkamutsatira Satana ndi bodza lake.

-Apa pali zimene Satana amkawawuza makolo athu kuti adzichita:

-Satana amkawawuza makolo athu kuti adzipembedza dzuwa, mwezi ndi nyenyezi.
-Satana amkawawuzanso makolo athu kuti adzipembedza mizimu.

-Makolo athu amkasema miyala ndi mitengo ndikumawoneka ngati anthu ndi nyama kuti adzizipembedza.

-Satana amkawatsogolera makolo athu kuti asamakhulupilire mwa Mulungu.
-Satana amkawatsogolera makolo athu kuti adzimuwukira Mulungu.

-Satana amkawatsogolera makolo athu kuti adzipembedza dzuwa, mwezi ndi nyenyezi.
-Satana amkawatsogolera makolo athu kuti adzipembedza mizimu.

-Satana safuna kuti wina aliyense adzipembedza Mulungu.

-Makolo athu samkafuna kuti Mulungu adziŵatsogolera.
-Makolo athu amkafuna kuti adzingomutsatira Satana yekha ndi anthu ena.

-Chigumula cha madzi chitatha, m'modzi mwa makolo athu amene anthu anamutsatira anali Nimulodi.

-Nimulodi anaŵalamula anthu kuti amange mizinda yambiri.

-Umodzi mwa mizinda imene anamanga anthu ndi wotchedwa Babulo.

-Mu mzinda wa Babulo, Nimulodi anaŵalamura anthu kuti amange msanja yayitali yokafika kumwamba kwa Mulungu.

Tiyeni tiŵerenge genesesi 11:1-4

1-Poyamba anthu onse a padziko la pansi amkalankhula chilankhulo chimodzi, ndipo mawu amene amkalankhulawo anali amodzi.
2-Atasamukira cha kuvuma, anakafika ku chigwa ku dziko la Sinara kumene anakhazikika.
3-Tsopano anayamba kuwuzana kuti,"Tiyeni tiwumbe njerwa ndikuzitentha." Motero m'malo mwa miyala anatenga njerwa, namangira phula m'malo mwa matope.
4-Ndipo anati, "Tsopano tiyeni timange mzinda wathu, ndipo msanja yake yitalike mpaka kukafika kumwamba. Tikatero tidzatchuka ndithu, ndipo sitizamwazikanso pa dziko la pansi."

-Mulungu anamuwuza Adamu ndi Nowa kuti achulukane pa dziko la pansi, ndipo adzikhala m'malo osiyanasiyana.



-Mulungu anawawuzanso anthu amene anabadwa mtsogolo mwa Nowa kuti achulukane pa dziko la pansi, ndipoadzikhala m'malo osiyanasiyana.

-Kodi chifukwa chiyani Mulungu samkafuna kuti anthu onse adzikhala pa malo amodzi?

-Mulungu samkafuna kuti anthu onse adzikhala pamodzi chifukwa chakuti samkafuna kuti iwowo amuyiwalire Iye.

-Mulungu samkafuna kuti anthu onse adzikhala pamodzi chifukwa chakuti samkafuna kuti machimo awo achuluke.

-Mulungu amkafuna kuti anthu adzikhala m'malo osiyanasiyana a pa dziko la pansi, koma anthu amkafuna kuti adzikhala pa malo amodzi.

-Anthu samkafuna kuti adzikhala m'malo osiyanasiyana a pa dziko la pansi.
-Anthu amkafuna kuti adzikhala pa malo amodzi pa dziko la pansi.

-Chomcho anthu onse anasamukira ku mzinda wa Babulo, ndipo anayamba kumanga msanja yayitali.

-Kodi chifukwa chiyani anthu anayamba kumanga msanja ku Babulo?

-Chifukwa chakuti anthu anali onyada kwambiri.
-Chifukwa chakuti anthu amkafuna kuti atchuke.

-Kodi Mulungu samkaŵawona anthuwo pamene iwo anayamba kumanga msanja yayitaliyo?